UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**


**KUYAMBIRA PA 20 JANUARY MPAKA PA 26 JANUARY 2025**

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

**Sabatayi ikuyembekezeka kukhala ya mvula m'madera ochuluka** kamba ka dera lodzetsa mvula la ITCZ mothandizana ndi mphepo za chinyontho zochokera ku Congo. Palinso, kuthekera kwakukulu kwa **dera la mpweya opepuka** kubadwa m'nyanja ya m'chere ya India ya pakati pa mayiko a Mozambique ndi Madagascar (yomwe imatchedwanso kuti Mozambique Channel) pafupi ndi doko la Beira cha kumathero a'sabatayi zomwe zikuyembekezeka kudzalimbikitsa nyengo ya mvula m'madera ambiri makamaka am'zigawo za pakati ndi kum'mwera. Zimenezi zikupereka **chiopsezo cha madzi osefukira mwadzidzidzi** m'madera otsika ndi malo ena omwe amasefukira madzi kawirkawiri.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali kwa nyengo ya mvula m'madera ena koma mvula yolozeka ku chigawo cha kum'mwera inagwa pa 16 ndi pa 17 January, 2025. Mapu ali m'musimu akuonetsa ena mwa madera omwe analandira mvula m'sabata yangothayi.




*Mapu: akusonyeza kagwedwe ka mvula kuyambira pa 15 January mpaka pa 17 January, 2025*

## MALANGIZO M'SABATALI

- **Madzi osefukira mwadzidzidzi:**Tikhale tcheru ndipo tipewe kuoloka madzi osefukira kapena othamanga kuti titeteze miyoyo yathu
- **Mvula ya Mabingu:** Kukamagwa mvula ya mabingu tikuyenera kubisala pamalo otetezeka bwino ndipo tipewe kubisala panso pa mitengo.
- **Chinyezi:** Tikhale osamala ndi **nyumba kapena zimbuzi** zomwe zanyowa kwambiri ndi mvula chifukwa zili pa chiopyezo chakugwa nthawi ina iliyonse.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:***

*The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 19 January, 2025**